

# Ndingatani Kuti Ena Azidziwa Kuti Nthawi Zina Ndimafuna Kuchita Zinthu Pandekha?



## NTHAWI YPOCHITA ZINTHU PANOKHA



### ZOMWE ZINACHITIKIRA ENA

Mtsikana wina dzina lake Allison ananena kuti: “Nthawi zina ndimangofuna kumachita zinthu pandekha. Koma azichemwali anga amandiona ngati kamwana ndipo amafuna kudziwa chilichonse chomwe ndikupanga. Sindikhala ndikubisa chilichonse, kungoti nthawi zina sindifuna kuti wina wake andisokoneze.”

N'chifukwa chiyani azichemwali ake a Allison amamuona ngati kamwana?

---

---

---

Kodi Allison angatani kuti azichemwali ake adziwe kuti nthawi zina nayenso amafuna atamachita zinthu payekha?

---

---

---

Mutakhala kuti **inuyo** ndinu Allison mungatani?

---

---

---



## KUCHIPINDA KWANU

### ZOMWE ZINACHITIKIRA ENA

Mnyamata wina dzina lake Ryan ananena kuti: “Zikakhala kuti tsiku limenelo sizina-ndiyendere, ndimangofuna kukhala ndekha. Ndikudziwa kuti n’zomveka kuti makolo azikudera nkhwawa, koma nthawi zina amangolowa kuchipinda pa nthawi imene sindikufuna kuti wina andisokoneze.

Kodi mukuganiza kuti makolo a Ryan amamudera nkhwawa?

---

---

---

Ngati ndi choncho mukuganiza kuti Ryan amachita chiyani (kapena sachita chiyani) zomwe zimachititsa kuti makolo ake azimudera nkhwawa?

---

---

---

Mutakhala kuti inuyo ndinu Ryan, **mungatani** kuti makolo anu azikukhulupirani?

---

---

---



## FONI YANU

### ZOMWE ZINACHITIKIRA ENA

Mtsikana wina dzina lake Nadine ana-nena kuti: “Mayi anga akangopeza kuti ndasi-ya foni yanga penapake, amayamba kuweringamo mameseji. Ulendo wina anasintha zinthu zina m’foni yanga kuti ndisamatumiziranenso mameseji ndi mnzanga wina chifukwa ankaona kuti sanali munthu wabwino kuti ndizicheza naye.”

Kodi mukuganiza kuti mayi ake a Nadine amadera nkhawa mwana wawo?

---

---

---

Ngati ndi choncho mukuganiza kuti Nadine amachita chiyani (kapena sachita chiyani) zomwe zimachititsa kuti mayi ake azimudera nkhawa?

---

---

---

Mutakhala kuti inuyo ndinu Nadine, **mungatani** kuti mayi anu azikukhulupirani?

---

---

---